

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa  
kuchokera m'Baibulo kupita kwa  
amene akulalikira Uthenga Wabwino

## CHILUNGAMO CHINAITANA NDIPO CHIFUNDO CHINAYANKHA

Afarisi anabwera ndi mai wina kwa Yesu. Iye anali atapezeredwa akuchita chigololo. Umboni wake unali wosakayikitsa. Chilango ndi chiweruzo zimamuyembekezera maiyu; ndipo chilango chake monga mwa lamulo chinali chotsimikizika. Komabe, Yesu, Mwana wa Mulungu, anamuza kuti: “Inenso sindikutsutsa iwe; pita; kuyambira tsopano usachimwenso” (Yohane 8:11).

Mu chaka cha 760 BC, kunali mzinda wina woipa wotchedwa Nineve. Kupanda umlungu, kupembedza mafano, kuchita zokhotakhota, ntchito zathupi, mabodza, kuononga, chiwawa, ndi ufiti zinafalikira mu likulu ili la ufumu wa Asiriya. Mulungu anatumiza mneneri Yona kukanena za chiweruzo cha Mulungu chimene chinali pafupi kuononga mzindawo. Mfumuyo ndi anthu ake analapa ndi kupempha kuti awachitire chifundo. Mulungu anaimitsa chiweruzo chake ndipo sanaononge mzindawo (Yona 3).

Pa Luka 15, Yesu akunena za nkhani ya mnyamata amene anapandukira atate wake. Mnyamatayu anachoka pakhomo nasiya zinthu zabwino naononga chuma chake chonse ndi moyo wachitaiko. Kenaka anakhala wosauka ndi wodetsedwa ndi uchimo. Atazindikira kuti sanachite bwino, ananyamuka ulendo wobwerera kwao, ndi cholinga chakuti akapemphe bambo ake kuti akamulandire ngati kapolo chabe. Bamboyo ankayang'anira kunjira kuti mwana waoyo abwerera liti ndipo atafika anamulandira ndi manja awiri. Mwana wolowererayu anakhululukidwa ndi kubwezeretsedwa pamalo ake aulemerero monga mwana wapakhomopo.

Nthawi zambiri, ana a Israele ankakana kumvera Mulungu ndipo amatsatira njira zao zauchimo. Kawirikawirinsu, Mulungu

amawakhululukira ndi kuwabwezeretsa. “Ndipo mwa nsoni zanu zochuluka simunawatha, kapena kuwataya; popeza Inu ndinu Mulungu wa chisomo ndi chifundo” (Nehemiya 9:31).

Panthawi ya kuweruzidwa ndi kupachikidwa kwa Khristu, Petro amene anali ophunzira wake anatsatira chapatali. Atafunsidwa ngati anali wotsatira wa Yesu, Petro anakana kuti samudziwa Ambuye. Iye anamukana Yesu katatu konse. Kachitatuko, Yesu anatembenuka ndi kumuyang'ana Petro amene anatuluka ndi kukalira modzimvera chisoni. Yesu atauka kwa akufa, anatumiza uthenga wapaderadera kwa Petroyo kuti amuuzze za kuuka kwake. Yesu anamukhululukira Petro, ndipo patapita masiku 50, Petro yemweyo anali kulalikira pa tsiku la Pentekoste.

Mfumu Davide anachita tchimo loopsa ndi Bateseba ndipo anamupha mwamuna wake kunkhondo. Pamene tchimo lake linaonekera poyera, Davide anapemphera kuti: “Mundichitire ine chifundo, Mulungu, Monga mwa kukoma mtima kwanu” (Salmo 51:1). Mulungu anamukhululukira Davide machimo ake.

Saulo, yemwe patsogolo pake anadziwika kuti Paulo Mtumwi, anapha ndi kumanga oyera mtima. Iye anali wankhanza ndi wozunza, komabe anachitiridwa chifundo pamene anazindikira Yesu ndiye Mesiya.

Chifundo cha Mulungu kwa anthu osakhala Ayuda chinaonekera ngakhale pomwe iwo sanalape. Mulungu anachedwetsa kubwerera kwa zidzukululu za Abrahamu kuti akalandire cholowa chao m'dziko la Kanani chifukwa mphulupulu ya Aamori inali isanafike pachimake (Genesis 15:16).

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Ndipo mwa nsoni zanu zochuluka simunawatha, kapena kuwataya; popeza Inu ndinu Mulungu wa chisomo ndi chifundo” (Nehemiya 9:31).

Mau a Mkonzi

Kalozera pophunzira  
Baibulo: Chifundo

Wolemera mu  
chifundo

Funso ndi Yankho

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

# ZIMENE BAIBULO

## LIMAPHUNZITSA ZA...

### Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

### Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

### Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

### Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;  
Aef. 2:1, 5-6

### Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

### Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

### Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;  
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

### Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

### Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;  
Akol. 1:18

### Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

### Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;  
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

### Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

### Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;  
1 Akor. 7:10-11

### Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

### Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;  
Mat. 25:31-46

### Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

### Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

### Kulalikira Uthenga Wabwino


Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Aamori anali ochimwa kwambiri, komabe Mulungu anaimitsa chiweruzo chake pa iwo pa kuwaonjezerako nthawi ndi chifundo.

Nkhani za m'Baibulo zifupizifupizi zili ndi zinthu zofanana komanso zolukanalukana. Izi zimapereka chithunzi cha chifundo chenicheni cha Mulungu. Chiweruzo chinali pafupi ndipo chilango chinali choyenera, komabe chifundo chinalowa m'malo mwa zonse.

Mulungu sanawapatse ndipo samapereka kwa anthu m'moyo uno zimene zikuwayenera, koma Iye ndi woleza mtima ndipo amawachitira chifundo. Dzanja lake lachifundo latambasulidwa kwa anthu onse mpaka lero. Iwo opanduka, ochimwa, oipa, ndi osayenera tsopano ali ndi chiyembekezo, pakuti Mulungu ali Mulungu wachifundo ndi wokhululukira.



Chifundo cha Mulungu chiyenera kulowerera ndikukhala gawo la miyoyo ya anthu onse. Mu 2007 bambo wina ankayenda ndi

banja lake pagalimoto. Anagundidwa ndi dalaivala woledzera. Bamboyo anatembenuka nkuona kuti ana ake awiri amene anali pampando wakumbuyo anali atafa. Mkazi wake yemwe anali woyembekezera, anali pampando pambali pake, nayenso anali atamwalira. Pamene ankayang'ana kudzera pagalasi losweka galimoto inayo yoyendetsedwa ndi dalaivala woledzera, anamva kuitana kwa Mulungu kuti amukhululukire ndikusiyana zonse. Iye anasonyeza chifundo ndi chikhululukiro kwa mnyamata amene anayendetsa galimoto ataledzera ndi kupha banja lake.

Zaka zambiri zapitazo, mbusa wa mpingo wa Mulungu anaphedwa mwankhanza. Wakuphayo anagwidwa ndi kuikidwa m'ndende. Banja la mbusayu lidachitira umboni kuti lidamukhululukira munthu yemwe adapha bambo waoyo.

Kodi ndi zolakwika zotani zomwe tachita zomwe zinali zoyenera kuti tilangidwe? Mwachimwira Mulungu motani? Kodi anthu ena apwetekeka bwanji chifukwa cha zochita zanu? Monga momwe Mulungu watikhululukira mwachisomo, ifenso tiyenera kuwakhululukira anthu amene atizungulira. Pamene anthu achita zinthu zoipitsitsa ndi kubweretsa zowawa m'miyoyo yathu, iwo angakhale osayenerera chifundo ndi chikhululukiro, komatu ifenso tinali osayenerera. Tiyenera tikhale oleza mtima ndi kusonyeza chifundo m'malo moweruza. Mulole anthu aone Mulungu mwa inu ndipo mukulitse chikondi chake kudzera mu chifundo chenicheni. Pamene ena akulirira chiweruzo, inuyo lilirani chifundo. Pamene ena akufuna kumudula munthu mumpingo, lilirani kuti abwezeretsedwe. Pamene ena akufunafuna chilango, funafunani kuti mubweretse machiritso.

Monga Atate wathu wa Kumwamba watichitira chifundo, ifenso tiyenera kuwachitira ena mwa chisomo chake. ■

*Gospel Truth* ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa [www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org) ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA  
[editor@thegospeltruth.org](mailto:editor@thegospeltruth.org)

# Mau a Mkonzi



*Chifundo ndi choonadi zisakusiye; Uzimange pakhosi pako; Uzilembe pamtima pako.*  
— Miyambo 3:3

Wokonedwa awerengi, ndikudandaulirani monga momwe anachitira Solomoni, “Chifundo ndi choonadi zisakusiye.” Nzodziwikiratu kuti dziko lathuli lili mumdima wandiweyani wa uchimo, ndipo mpofunika kuti kuunika kwa choonadi kuwale kwambiri. Kangamirani ku choonadi ndipo muyende nacho, koma osati choonadi chokha. Mukangamirenso chifundo. Chifundo cha Mulungu ndi chimene chinatipulumutsa, ndipo chifundo chimene timaonetsera ena chomwe chidzawalozere iwo ku chiyembekezo chimene chili mwa Khristu Yesu.

Mutu wa ulendo uno ndiwo 'Chifundo.' Ndinakhudgidwa mtima kwambiri pamene ndimawerenga malemba ndi kulingalira za mutu umenewu. Pali mavesi ochuluka amene amaphunzitsa ndi kusonyeza za kuyenera ndi kufunikira kwa chifundo. Nkofunika kudziwa kuti pali zambiri zimene zimanenedwa zokhudza kufunika kwa chifundo kuposana ndi zambiri mwa ziphunzitsa zimene anthu ena amazitsatira. Monga taonera pamwambapa, tiyeni tikangamire ku choonadi, koma tiasiyeye chifundo.

Popanda chifundo cha Mulungu, palibe aliyense wa ife amene akanapulumutsidwa. Ifeyo sitinali oyenera chikondi cha Mulungu komabe Iye anatikonda. Ngakhale pamene tayamba ulendo wathu mwa Ambuye, chifundo chake ndi chomwe chimatisunga, chifukwa tonse timalakwitsa ndi kupotoza. Moyo wachipambano ndiwo muyezo wa Baibulo, ndipo kalata walembedwayu sakufuna kuti tikhale m'moyo wotayirira ndi wopeputsidwa; KOMABE ndi angati a ife amene sitinafunepo kubwerera kwa Yehova ndi kumpempha kuti atikhululukire? Ndinapulumutsidwa ndi chifundo chake, ndipo ndili pano lero chifukwa cha chifundo chachisomo chimene wanditambasulira ine chifukwa cha zolakwa ndi zofooka zanga. Popeza kukhala ndi moyo kwa Mulungu ndi moyo wakuti tidzikula, nthawi zonse padzakhala malo amene tidzafunikira chifundo chake.

Pamene ndikulingalira za chifundo chimene Mulungu wakhala akuwachitira kwa anthu kwa zaka zonsezi, ndimadabwa komanso ndimatsutsidwa pamoyo wanga. Ndimakumbukira bwino lomwe ndikubwerera kuchokera ku ulendo wokatumikira ndipo ndimaganiza kuti, “Ndamaliza. Sindidzabwereranso kwa anthu akuthupi awa.” Mulungu analankhula nane nandikumbutsa za fanizo la mkuyu lolembedwa pa Luka 13. Mulungu anali asanathane nane, ndipo ndinasuzumira kuzama kwa chifundo chake. Komabe, chifundo changa chinaonjezedwa ndi chisomo chake.

M'dziko lachipembedzo, mudzapeza mayanjano ambiri opanda malamulo okhwima, osagwirizana ndi chikondi ndi chifundo pamene akuphunzitsa choonadi chochepa. Kumeneko ndi kulakwa. Ndi kulakwanso pamene tikweza mbendera ya choonadi ndi chiyero popanda mzimu wachifundo. Pamene mudzi wina wa Asamariya unamukaniza Khristu kuti asawayendere, ophunzirawo anafuna kuti moto utsike ndi kuwaotcha onsewo. Yesu anati, “Simudziwa kuti muli a mzimu wotani” (Luka 9:55). Ndaona mzimu woweruza mwa anthu ambiri amene amadziona kuti ndi “oyera”. Pamene anthu ena ali ndi chizolowezi choyeza ena motsutsa, pamene pakusoweka chikondi ndi chifundo. Chinthu chosautsa nchakuti zikhoza kukhala zovuta kuwachitira chifundo anthu okhala ndi mtima oweruza anzawo.

Kukhala achifundo ndi mdalitso ku miyoyo yathu komanso ya ena. Chifundo chimaposa chiphunzitsa; ndipo kugwiritsa ntchito kwenikweni kwa chikondi, kukhululukira, kuleza mtima, kufunafuna chiyanjanitso, ndi zina zotero. Mulungu atithandize ife tonse kuyesetsa kukhala achifundo chochuluka ndi osakonda kuweruza ena popanda kusiya choonadi.

Michael W. Smith

April 2024

## PITANI NDI KULOWA /PA APP

Nkhokwe yaikulu yophunzirira Baibulo ndi kumvetsetsa ziphunzitsa za Baibulo.



*Mukafuna kutipeza*

*pa intaneti, mulembe*

*www.thegospeltruth.org*

*kuti mudzilandira makalata*

*athu kapenanso kuti*

*muone makalata akale.*



# Kalozera pophunzira Baibulo

## Mutu: Chifundo

**Mau a Mulungu:** *Koma Inu, Ambuye, ndinu Mulungu wasoni ndi wachisomo, Wosapsa mtima msanga, ndi wochulukira chifundo ndi choonadi. — Salmo 86:15*

**Tanthauzo:** Chifundo ndicho “kukhala wokoma mtima ndi wokhulukira; chimene chimatikakamiza kuti tichite chifundo; kulekerera ndi mtima wa chisoni woonetsedwa kwa olakwa kaya ndi munthu kapena bungwe amene apatsidwa udindo wopereka chilungamo” (Vocabulary.com).

**Mwachidule:** Mulungu ali wodzala chifundo ndi kukoma mtima ndipo amachedwetsa popereka chiweruzo, pofuna kupereka mwai kwa anthu kuti akhulukidwe ndi kubwezeretsedwa. Momwemonso ana a Mulungu akuyenera kuyanjana ndi kulumikizana ndi ena kuchokera ku tsinde ndi mzimu wachifundo.

### I. Chikhalidwe chaumulungu cha Mulungu

- A. 2 Akorinto 1:3-4 Mulungu, Atate wa zifundo.
- B. Daniele 9:9 Chifundo ndi chikhulukiro ndi za Mulungu.
- C. Duteronomo 4:29-31 Mulungu ali Mulungu wachifundo.
- D. Mika 7:18 Mulungu amakondwera ndi chifundo.
- E. Mateyu 9:36 Yesu anagwidwa chifundo.

### II. Chifundo cha Mulungu nchochuluka ndiponso nchokhalitsa

- A. Salmo 103:8 Yehova ndi wachifundo chochuluka.
- B. Salmo 51:1-2 Chifundo chokoma.
- C. 1 Mbiri 16:34 Chifundo chake chikhala chosatha.
- D. 2 Petro 3:9 Osafuna kuti ena aonongeke.

### III. Onse anachimwa ndipo akuyenera kuweruzidwa

- A. Aroma 3:23 Pakuti onse anachimwa.
- B. Aroma 6:23 Mphotho yake ya uchimo ndi imfa.

### IV. Chifundo ndi chosayenera ndipo chili chifuniro cha Mulungu

- A. Aefeso 2:4-6 Chifundo sichiyenera kwa ife.
- B. Aroma 9:15-16 Chifundo nchogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu.

### V. Chipulumutso ndi moyo wosatha molingana ndi chifundo

- A. Luka 1:78-79 Kuwala kwa Uthenga Wabwino kunabwera ndi chifundo cha Mulungu.
- B. Tito 3:4-7 Chipulumutso osati monga mwa ntchito koma mwa chifundo.
- C. Yesaya 55:7 Mulungu amakhulukira oipa.
- D. 1 Petro 1:3-4 Chifundo cha Mulungu chimabweretsa chiyembekezo cha Kumwamba.

### VI. Chifundo chimagwiriziza anthu a Mulungu

- A. Salmo 94:18 Chifundo chigwiriziza iwo amene aterereka.
- B. Maliro 3:21-23 Ndi chifundo cha Yehova kuti sitinathedwe.

### VII. Mkulu Wansembe wachifundo

- A. Ahebri 2:16-18 Yesu ndiye mkulu wansembe wachifundo.
- B. Ahebri 4:15-16 Chifundo chopezeka pampando wachifumu wachisomo.

### VIII. Mapeto a chifundo cha Mulungu

- A. Yohane 12:48 Chiweruzo pa iwo amene akukana.
- B. Mateyu 25:45-46 Chilango chosatha kwa osakhulupirika.
- C. Ahebri 10:28-29 Kufa wopanda chifundo.

### IX. Kuitanidwa ku moyo wachifundo

- A. Luka 6:36 Khalani achifundo monga Mulungu ali wachifundo.
- B. Mika 6:8 Kondani chifundo.
- C. Zekariya 7:9 Onetsani chifundo ndi kukoma mtima.

### X. Chifundo ndi chabwino kuposa nsembe

- A. Mateyu 23:23 Tsoka kwa iwo amene salabadira chifundo.
- B. Hosea 6:6 Mulungu amafuna chifundo kuposa nsembe.
- C. Mateyu 9:11-13 Yesu amafuna chifundo osati nsembe.

### XI. Madalitso ndi chiweruzo

- A. Mateyu 5:7 Odala ali akuchita chifundo.
- B. Yakobo 2:13 Chiweruzo chopanda chifundo pa iwo amene alibe chifundo.
- C. Mateyu 18:33-35 Khulupirirani zochimwa.

### Kumaliza

*Chifukwa chake valani, monga osankhika a Mulungu, oyera mtima ndi okonedwa, mtima wachifundo, kukoma mtima, kudzichepetsa, chifatso, kuleza mtima; kulolerana wina ndi mnzake, ndi kukhulukirana eni okha, ngati wina ali nacho chifukwa pa mnzake; monganso Ambuye anakhulukira inu, teroni inunso. — Akolose 3:12-13*



# WOLEMERA MU CHIFUNDO

Anthu ambiri amaona kuti Mulungu ali ndi lupanga lake lachiweruzo lokwezedwa lokonzekera kudula anthu chifukwa cha kulakwa kulikonse kwauzimu. Kumvetsetsa kumeneku kwa Mulungu sikoona ayi, pakuti Mulungu ndi wachifundo. Manja ake achifundo amatambasulidwa kuthandiza aliyense mu nthawi yake ya uchimo, kulephera, kusowa, kuvutika, ndi mayesero.

## Khalidwe laumulungu la Mulungu

Davide polemba Salmo anati: “Koma Inu, Ambuye, ndinu Mulungu wansoni ndi wachisomo, Wosapsa mtima msanga, ndi wochulukira chifundo ndi choonadi” (Salmo 86:15). Chifundo ndi khalidwe lokoma mtima ndi lokhululuka. Ndi chikhaliidwe chimene chimakhudzana ndi chisoni, kukhululuka, ndi kulekerera pamene pakanakhala

“Mulungu ndi wolungama ndi woyera, komabe chikhululuko ndi chifundo zili zake. Chifundo ndi gawo lofunika kwambiri la chikhaliidwe chake, pakuti Iye ndiye anachiyambitsa.”

chiweruzo. Chifundo, monga gawo locheperapo la chisomo, ndiyo mphatso ya chikondi ndi chifundo cha Mulungu pamene satilanga moyenera ndi kulakwa kwathu.

Chifundo cha Mulungu nthawi zambiri chimanyozedwa ndi kupeputsidwa. Mulungu ali “Mulungu wa chitonthozo chonse” komanso “Atate wa zifundo” (2 Akorinto 1:3). Chifundo ndi chikhaliidwe chofunika kwambiri cha Mulungu. “Ambuye Mulungu wathu ndiye wachifundo, ndi wokhululukira”

(Daniele 9:9). Mulungu ali wolungama ndi woyera, komabe chikhululuko ndi chifundo zili zake. Chifundo ndi gawo lofunika kwambiri la chikhaliidwe chake, pakuti Iye ndiye anachiyambitsa.

Malemba amafotokoza mobwerezabwerezwa ndi kupereka chitsanzo cha chifundo cha Mulungu mu zochita zake ndi anthu. Pamene anthu ali m'mavuto ndi kufunafuna Yehova, Iye sadzawasiya, “popeza Yehova Mulungu wanu ndiye Mulungu wachifundo” (Duteronomo 4:31). Anthu akakhala m'mavuto ndi kufunafuna Yehova, iye sadzawasiya. Pa Mika 7:18, mneneriyu analemba momveka bwino kuti: “Ndani Mulungu wofanana ndi Inu, wakukhululukira mphulupulu, wakupitirira zolakwa za otsala a cholowa chake? Sasunga mkwiyo wake ku nthawi yonse popeza akondwera nacho chifundo.” Khristu anaulula mbali imeneyo ya chifundo pamene anatomikira ochimwa pa nthawi imene anali pa dziko lino lapansi. “Poona makamuwo, anagwidwa m'mtima ndi chisoni” (Mateyu 9:36).

## Chifundo cha Mulungu nchochuluka ndiponso nchokhalitsa

Mulungu ali “Wosakwiya msanga, ndi wa chifundo chochuluka” (Salmo 103:8). Pali nyumba yodzadza ndi chifundo yomwe imaposa chiweruzo. Davide analilira pa chifundo chimenecho pamene adachimwa ndi Bateseba. Davide anali wosweka mtima, wolakwa, ndi wolapa. Iye anapemphera kuti, “Monga mwa unyinjira wa nsoni zokoma zanu, mufafanize machimo anga” (Salmo 51:1). Chifundo chimatanthauza kuti Mulungu ali wokonzeka, wamkulu, ndi wololera kuti atikomere mtima. Pempho la Davide silinali lofuna chilungamo, koma chiyembekezo chake chinali mwa chifundo cha Mulungu chopanda malire. Mwa chifundo chake, Mulungu akuchedwetsa chiweruzo chomaliza kuti apatse anthu mwai wochulukira woti apulumuke. Ambuye “aleza mtima kwa ife, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa” (2 Petro 3:9).

## Onse anachimwa ndipo ayenera kuweruzidwa

“Pakuti onse anachimwa” (Aroma 3:23), analakwa, ndipo anaswa malamulo a Mulungu. Chifukwa cha uchimo umenewu, tonsefe ndife oyenera kulangidwa, pakuti “mphotho yake ya uchimo ndi imfa;” (Aroma 6:23). Komabe, tili mu chikhaliidwe chathu chosayenera, Mulungu anakulitsa chikondi ndi chifundo chake kupyolera mwa Yesu Khristu, “koma Mulungu, wolemera chifundo, chifukwa cha chikondi chake chachikulu chimene anatikonda nacho, tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Khristu (muli opulumutsidwa ndi chisomo)” (Aefeso 2:4-6). Chifundo sichibwera ndi chifuniro cha munthu koma cha chifuniro cha Mulungu wamphamvuzonse (Aroma 9:15-16). Munthu sali woyenera ndipo sangachipeze chifukwa wachita zoyenera. Chifundo ndi mphatso yochokera kwa Mulungu.

## Chipulumutso ndi moyo wamuyaya molingana ndi chifundo

Chinali chifukwa cha chikondi kuti Mulungu anatomiza Yesu kudzafera machimo a anthu. Chipulumutso chinadza, “zosati zochokera m'ntchito za m'chilungamo, zimene tidazichita ife, komatu monga mwa chifundo

*(Yapitirira pa tsamba 6)*

(Kuchokera pa tsamba 5)

chake anatipulumutsa ife” (Tito 3:5). Chipulumutso sichimaperekedwa kwa iwo amene ali oyenerera mwa ubwino ndi kulungama kwao. Chipulumutso chimaperekedwa mwa chifundo kwa ochimwa oipitsitsa amene angalape ndi kulandira mphatso iyi ya Mulungu. Pamene oipa asiya njira zao nabwerera kwa Yehova,



**“Akhristu sayenera ‘kuchitira’ chifundo chabe, koma ayenera ‘kukonda’ chifundo. Chifundo sichimangoyang’ana mmene munthu akumvera kapena kungoganizira zofuna za ena.”**

“adzamchitira chifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye adzakhululukira koposa” (Yesaya 55:7). Munthu amene amadziona kuti ali wosayerenera chikondi ndi chikhululukiro cha

Mulungu chifukwa cha zolakwa zake zakale adzalandiridwa ndi kuyanjanitsidwa ndi Mulungu chifukwa cha chifundo chake.

### **Chifundo chimachirikiza anthu a Mulungu**

Davide analemba kuti: “Literereka phazi langa, Chifundo chanu, Mulungu, chinandichirikiza” (Salmo 94:18). Kwa anthu amene akufunafuna kutumikira Mulungu, nthawi zina amalephera komanso

amalakwitsa zinthu. Mulungu sadzachotsa munthu akalephera kukhala wangwirowo; koma adzamuthandiza ndi kumukonzanso. Mulungu ndi Yemwe amatsitsimutsa anthu ndi chifundo chake kuopa kuti angaonongeke. Moyo ukakhala wamdima ndipo zinthu zikaoneka kuti ndi zosatheka, kumbukirani mneneri Yeremiya amene anati, “Ndili nacho chiyembekezo popeza ndilingalira ichi ndiyembekeza kanthu. Chifukwa chakusathedwa ife ndicho chifundo cha Yehova, pakuti chisoni chake sichileka; Chioneka chatsopano m’mawa ndi m’mawa” (Maliro 3:21-23).

### **Mkulu Wansembe wachifundo**

Yesu anasanduka munthu, “kuti akadzakhala mkulu wa ansembe wachifundo ndi wokhulupirika” (Ahebri 2:17). Amamvetsetsa zovuta za thupi ndipo amachitira chifundo anthu m’mavuto ao. Anthu akhoza kupita ndi chitsimikizo kwa wansembe wamkulu ameneyo, ndi “kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa” (Ahebri 4:16).

### **Mapeto a chifundo cha Mulungu**

M’moyo uno, Mulungu ali wokonzeka kuchita chifundo kusiyana ndi kupereka chiweruzo. Kungakhale kulakwa, kusalabadira zoonadi za chiweruzo chimene chikubwera pamene chifundo cha Mulungu chidzathe. Chiweruzo chidzafika kwa iwo amene akana Yesu ndi mau ake (Yohane 12:48). Padzakhala chilango chamuyaya (Mateyu 25:45-46) kwa iwo amene akana kulandira

chifundo cha Mulungu ndi chipulumutso. Monga iwo amene ananyoza chilamulo cha Mose anafa wopanda chifundo, momwemonso adzachitire iwo akunyoza mwazi wopulumutsa wa Yesu (Ahebri 10:28-29).

Tamandani Mulungu chifukwa cha chifundo chake! Kupyolera mu chikondi ndi chikhululukiro chake, pamene tilapa, m’malo mwa chilango chimene tikuyenera kulandira, tingapeze chiyembekezo, mtendere, ndi kubwezeretsedwa. Mulungu alibe tsankho, ndipo chifundo chake chimafikira anthu onse, mosasamala za chiyanambi chao ndi mavuto ao.

### **Kuitanidwa ku moyo wachifundo**

Monga Mulungu ali wachifundo, momwemonso otsatira ake ayenera kukhala achifundo. Yesu anapereka malangizo omveka bwino amene ayenera kutsatiridwa: “Khalani inu achifundo monga Atate wanu ali wachifundo” (Luka 6:36). Yesu anapereka malangizo omveka bwino amene ayenera kutsatiridwa. Mika 6:8 akufunsa kuti: “Yehova afunanji nawe koma kuti uchite cholungama, ndi kukonda chifundo...Akhristu sayenera ‘kuchitira’ chifundo chabe, koma ayenera ‘kukonda’ chifundo. Chifundo sichimangoyang’ana mmene munthu akumvera kapena kungoganizira zofuna za ena. Chifundo m’maonekedwe ake angwirowo sichimanyinyirika kapena kukakamiza koma ndi chochulukira ndi chochokera mu mtima.

### **Chifundo chiposa nsembe**

Ngakhale kuti pali nthawi ya chiweruzo cholungama, mwana wa Mulungu akuyenera kuika mtima kwambiri pa kusonyeza chifundo kwa anthu amene akukhala moyo umene zambiri zimawavutirapo. Monga amachitira Afarisi, Akhristu ambiri amasamala kwambiri chiyero choonekera kunjani ndipo amanyalanyaza zofunikira kwambiri za zachifundo (Mateyu 23:23). Chipangano Chakale (Hoseya 6:6) ndi Chipangano Chatsopano (Mateyu 9:11-13) chomwe zonse zimatsimikiza kuti Mulungu amakonda kuchita chifundo kuposa nsembe. Mzimu wachifundo ndi WOFUNIKIRA kwambiri kuposa nsembe zakunja za moyo woyera. Chiweruzo chimasendera zinthu kutali pomwe chifundo chimachonderera ndikupereka mwai wosintha.

Pamene anthu alakwitsa kapena kuchimwa, oyera mtima akuyenera kuwalankhula ndi kuchita nawo mwachifundo ndi mokhululukira. Tonsefe timafunikira ndipo tikadafunabe chifundo cha Mulungu. Kodi ana a Mulungu angakhale bwanji opanda kuwachitira chifundo ochimwa ngakhalenso ndi ena odzitcha Akhristu?

### **Madalitso ndi chiweruzo**

Yesu anati: “Odala ali akuchitira chifundo; chifukwa adzalandira chifundo” (Mateyu 5:7). Ngati mwana wa Mulungu sakhala moyo wochitira ena chifundo, Mulungu adzamuweruza mopanda chifundo (Yakobo 2:13). Ngati otsatira a Khristu sakhululukira anthu m’zolakwa zao ndi kufunafuna kubwezeretsedwa, Mulungu naye sadzawakhululukira (Mateyu 18:33-35).

Tikufunitsitsa chifundo cha Mulungu m’miyoyo yathu, ndipo tiyenera kukhala ofunitsitsa kukulitsa chifundo chimenecho kwa omwe akutizungulira. ■



## Kodi ndingasonyeze bwanji chifundo pamene wina akundidyera masuku pamutu?

Kukhala ndi mzimu wachifundo sikutanthauza kuti mumalola anthu adzingokuzunzani mmene angafunire. Ngati wina wandimenya, ndiyenera kumpatsanso tsaya lina monga momwe Yesu anaphunzitsira. Mwa njira ina, sindiyenera kubwezera, koma ndipirire kupwetekako; ndipo ngati nkotheke ndichokepo. Pamene khamu la anthu linkafuna kuponya Yesu ku mbali kwa phiri, Iye anathawa.

Ngati wina akukudyerani masuku pamutu ku gawo lakuthupi, la zachuma, kapena m'magawo ena, mpofunika kuzindikira chimene malemba amanena pa zonse. Gawo la chifundo ndilo la kukhululukira munthu amene wamulakwira. Tiyenera kupereka munthu ameneyo kwa Yehova ndi kumukhululukira kotheratu, posatengera kuti watilakwira kangati. Komabe, zimenezo sizikutanthauza kuti tiyenera kuitana chigawenga m'nyumba mwathu pamodzi ndi ana athu kapenanso kupereka makiyi a chitseko chatu kwa wakuba. Tiyenera kukhala adindo abwino a zimene Mulungu watipatsa. Nthawi zina izi zikutanthauza kukweza muyezo wa chiweruzo ndikukhazikitsa mfundo ndi ndondomeko zomwe zimayenera kutsatidwa. Pa nthawi imeneyo, timayenera kuchita zinthu zonse ndi mtima wachikondi. Pamene chilungamo chikusowa m'dziko, tiyenera kudziwa kuti chifundo chilibe mphamvu yoyanjanitsa, koma chimapangitsa kuti chiyanjano chitheke.

## Kodi mumalumikizitsa bwanji kukhala ndi muyezo wa choonadi ndi kuchitira ena chifundo?

Moyo wanga uli m'dzanja langa. Ndiliba mphamvu yosintha anthu ena, koma ndili ndi mphamvu mwa chisomo kukhala moyo woyera ndi wa choonadi pamaso pa Mulungu. Sitiyenera kunyalanyaza chilungamo m'miyoyo yathu chifukwa cha anthu ena otizungulira. Gawo la muyezo wa choonadi likanakhala kuchitira chifundo ena amene moyo wao ndi wosalungama. Tiyesetse kwambiri pa kuonetsera chikondi kwa ena amene sakukhala m'moyo waumulungu.

Mfundo yofunika kwambiri kuti Akhristu aphunzire ndiyo yakuti kuvomereza sikutanthauza kuti walola. Titha kuvomereza munthu ndi kumukonda koma osalolera zimene akuchita. Tangoganizani kuti ngati palibe choonadi chogwirika, palibenso chifundo chakuti chiperekedwe. Chifundo sichifunikira kwa iye amene akuchita zonse molondola; koma ndi chofunika kwa iye amene akulakwitsa.

Lemba la Salmo 85:10 limati: "Chifundo ndi choonadi zakomanizana; chilungamo ndi mtendere zapsomponana." Choonadi cha chilungamo chimavumbulutsa uchimo ndipo chimafuna chiweruzo. Pamene mbali inayi chifundo chimafunafuna mtendere ndi kubwezeretsedwa. Kudzera mwa Khristu, choonadi ndi chifundo zinakumana pa mtanda, ndipo pamalo okumaniranapo ifeyo tinapeza chipulumutso. Tikufuna kuti chifundo ndi choonadi zilumikizansenso m'miyoyo yathu. Lalikirani, phunzitsani ndipo khalani m'choonadi kuti ena akhoza kuona njira ya choonadi; komabe muwachitire chifundo ndi chisoni mu kusokera kwao. Chifundo chimenecho ndi chimene chidzawakokere ku choonadi, osati mzimu wa kudzilungamitsa.

Choonadi ndi chifundo, kapena chiweruzo ndi chifundo, siziyendera limodzi. Kukhala ndi chiweruzo cholungama, monga Khristu anaphunzitsira, sizimachota kuchita chifundo.



Mayendedwe onse a Yehova ndiwo chifundo ndi choonadi kwa iwo akusunga pangano lake ndi mboni zake. —Salimo 25:10

Monga momwe njira kapena khwalala zopangidwa ndi matayala angolo zimazindikirika mosavuta, momwemonso akuyenera kukhalira mayendedwe achifundo ndi choonadi zomwe zimatitsogolera kwa Khristu. Akhristu sakuyenera kungovomereza njira ya choonadi komanso njira yachifundo.



*Zizindikiro zosonyeza kuti mukuweruza ena:*

1. Pamene mwakumana ndi anthu, mumawaunguza kotheratu.
2. Mumadziona olungama ndipo mumakwiya kwambiri ndi zolakwa kapena machimo a ena kuposana ndi zoipa zanu.
3. Simuwakhulukira anthu mwansanga akakulakwirani.
4. Mumanyozera ndi kudzilekanitsa nokha kwa anthu omwe mumatsutsana nawo kapena ndi osiyana ndi inu.
5. Ndinu omasuka kuyankhula mosavuta za momwe mumaonera zosowa za anthu ena kapena zofooka zao zauzimu.
6. Simuvutika kuti muone zolakwa za ena.



## YANJANANI KUCHOKERA KU MPANDO WACHIFUNDO

### Kuti Mutipeze

The Gospel Truth  
P. O. Box 2042  
Nixa, MO 65714  
USA

Email:  
editor@thegospeltruth.org

*Ndipo pomwepo ndidzakomana ndi iwe, ndi kulankhula ndi iwe, ndiri pamwamba pa chotetezerapo. — Eksodo 25:22*

Panthawi imene Aisraele anali kuyendayenda m'chipululu, ananyamula chihema, kachisi onyamulika. Likasa la Chipangano linaikidwa m'Malo Opatulikitsa, amene anali chipinda chamkati cha chihema. Pamwamba pa likasalo panali chovundikira chimene chinkatchedwa Malo achifundo.

Pamenepa ndi pomwe Mulungu ankayankhulana ndi Mkuluwansembe kamodzi pachaka pa Tsiku lochita Chotetezera. Ndi chinthu chokoma ndi chodala kudziwa kuti Mulungu analumikizana

ndi anthu ake kuchokera ku mpando wachifundo osati kuchokera ku mpando wakuweruza. Ziliba kanthu kuti tchimolo linali loopsa motani, koma pamene mwazi unapapidwa, Mulungu anatambasula chifundo ndi chikhulukiro kwa ana a Israele.



### CHIYERO CHA KWA AMBUYE



Ngakhale kuti mwazi wa ng'ombe zamphongo ndi mbuzi unali wopanda ungwiro kuti uchotse uchimo, Yesu anafa pa mtanda kuti akachotse uchimo wa anthu onse. Mu nyengo ya Chipangano Chatsopano ichi, tikhoza kuyandikira kumpando wachifumu wa Mulungu kumene adzalankhula nafe kuchokera ku mpando wachifundo ndi chikondi. Ngati pali tchimo kapena kulephera, munthu akhoza kubwera kwa Khristu, amene kudzera mu chifundo chake, ali ngati ulalo wotilumikizitsa ndi Mulungu. M'malo moweruza ndi kuononga, Iye adzapereka njira ya machiritso ndi chiyanjantiso. Sityenera kuchita mantha poyandikira mpando wachifundo wa Mulungu, chifukwa kumeneko ndi kumene tingalankhule ndi Mfumu ya mafumu.

Ndife odala kukhala ndi mwai ndi chitsimikizo choyankhulirana ndi Mulungu kuchokera kumpando wachifundo. Ife monga ana a Mulungu timayanjana ndi anthu ambiri pamoyo wathu monga abale, anansi, akhristu anzathu, ogwira nawo ntchito ena otero. Kodi timayankhula nawo kuchokera pampando wotani? Kodi tikulankhula ndi kupanga zisankho m'miyoyo yathu kuchokera kumpando wachiweruzo kapena kumpando wachifundo?

Tiyenera kuyenda m'mapazi a Yesu ndipo tikhale otenga nawo gawo mu chikhalidwe chake chaumulungu. Ngati Mulungu alankhula nafe kuchokera kumpando wachifundo, tingakhalenso bwanji aukali ndi oweruza muzochita zathu ndi mzimu wathu ndi anthu ena? Tiyeni tilankhule ndi anthu onse mwachifundo kuti athe kuona Yesu ndikupeza njira yochiritso ya chiyanjantiso. ■